# KALOZERA WA UFULU WANU

## Mtolo wa Ufulu wachibadwidwe ku Malawi




KONRAD ADENAUER STIFTUNG
RULE OF LAW PROGRAM FOR ANGLOPHONE SUB-SAHARAN AFRICA

Centre for Human Rights
UNIVERSITY OF PRETORIA

A Guide to Your Rights: The Malawi Bill of Rights
ISBN: 978-1-991213-10-5
© 2021
Centre for Human Rights, University of Pretoria

Designed by Judava Worx

**The Centre for Human Rights**, Faculty of Law, University of Pretoria, is an internationally recognised university-based institution combining academic excellence and effective activism to advance human rights, particularly in Africa. It aims to contribute to advancing human rights, through education, research and advocacy.
www.chr.up.ac.za

**Konrad Adenauer Foundation** (**KAS**) is a German Political Foundation that is committed to achieving and maintaining peace, freedom and justice through political education on a national level as well as on an international level with 111 offices worldwide. The KAS Rule of Law Program for Anglophone Sub-Saharan Africa based in Nairobi has been actively promoting the rule of law, democracy and human rights in the region since 2006. Strengthening constitutionalism as well as the enforcement of basic human rights enshrined in the constitutions of Sub-Saharan Africa has always been among the main focus of the Program's work.

# MAU OTSOGOLERA

Mbiri ya ufulu wachibadwidwe idafalikira ponseponse m'Malawi muno ndipo pafupifupi aliyense adamvako momwe ufulu wachibadwidwe umathandizira kutukula miyoyo ya anthu. Ufulu wachibadwidwe umaperekedwa kwa aliyense mdziko lino la Malawi pomupatsa danga lokamang'ara ku khothi ngati ufulu wake waponderezedwa. Ndikovuta kuti anthu omwe sadziwa za ufulu wawo adyerere ufuluwo mokwanira popeza mwazina sangadziwe katetezedwe ka ufuluwo. Kabuku kano kalembedwa kuti kakuphunzitseni tsatanetsatane wa ufulu wanu ndi katetezedwe kake.

Kabuku kano kakufotokozera mwamvemvemve za ufulu wachibadwidwe, mbiri yake, komanso tanthauzo lake kwa nzika ndi anthu onse okhala m'Malawi. Bungwe la Centre for Human Rights (yomwe ndi nthambi ya Yunivesite ya Pretoria ku South Africa) ndi bungwe la Konrad –Adenaue - Stiftung (KAS) agwirizana zosindikiza kabuku kano pofuna kuunikira anthu onse a m'Malawi muno, za ufulu wachibadwidwe ndi cholinga chopititsa patsogolo ntchito yomenyera ndi kuteteza ufulu kuti usaponderezedwe ndi boma, mabungwe omwe siaboma komanso ndi anthu kumene.

Mabungwe a Centre for Human Rights ndi a Konrad-Adenauer- Stiftung ali ndi cholinga chothandiza kupititsa patsogolo ufulu wachibadwidwe womwe umathandiza kutukula miyoyo ya anthu. Mabungwewa akukhulupirira kuti ufulu wachibadwidwe udzazikizira anthu akadziwa za ufulu wawo. Tikhulupilira kuti kabuku kano ndi kalozera yemwe adzaunikire anthu za m'mene angamenyerere ufulu wawo wachibadwidwe womwe uli m'Malamulo aakulu adziko la Malawi (Constitution).

Prof Frans Viljoen

Director
Centre for Human Rights

University of Pretoria

Dr. Stefanie Rothenberger

Director
Rule of Law Program for
Anglophone Sub-Saharan Africa
Konrad-Adenauer-Stiftung

Mawu Oyamba 1

Kodi malamulo akulu ndi chiyani? 2

Mbiri ya Malamulo a Akulu adziko la Malawi 4

Zamkati mwa m'Malamulo a Akuluwa 8

Mgawikano wa ntchito ndi mphamvu wa nthambi zitatu zaboma 9

Mndandanda makhothi ku malawi 11

Maziko a ufulu wachibadwidwe 13

Mtolo wa ufulu wachibadwidwe 17

Mndandanda wa mtolo wa ufulu wachibadwidwe 18

Kutambasula mtolo wa ufulu wachibadwidwe mwachidule 19

Kuumba mkota 31

Mabungwe oteteza muteteze ufulu wachibadwidwe 32

# ZAMKATIMU

# MAWU OYAMBA

M'Malawi aliyense ali ndi ufulu wachibadwidwe womwe umamuteteza ndipo cholinga chake ndi kumuthandiza kukhala moyo wabwino komanso watanthauzo. Ufuluwu umapezeka m'Malamulo a akulu oyendetsera dziko la Malawi (Constitution) mgawo lokamba za Mtolo wa Ufulu Wachibadwidwe (Bill of Rights).



(CREDIT: Swathi Sridharan (ICRISAT))


## Kagwiritsidwe ntchito ka kabukuka

Cholinga cha Kabukuka ndi kulongosola za Malamulo a Akulu oyendetsera dziko la Malawi, kuti mudziwe zomwe malamulowo amanena pa ufulu wanu wachibadwidwe. Kabukuka kafotokozera za ufulu wachibadwidwe pogwiritsa ntchito milandu yomwe idaweruzidwapo kale ku makhothi pomwe anthu ndi mabungwe osiyanasiyana adakamang'arira anthu anzawo kapena boma ndi nthambi zake pamene ufulu wawo wachibadwidwe udaponderezedwa.

Kabukuka kakungokupatsani chinthunzithunzi cha mtolo wa chibadwidwe omwe uli m'Malamulo a Akulu woyendetsera dziko. Ngati mukufuna kuwerenga Malamulo a Akulu woyendetsera dziko la Malawi mwatsatanetsane, pitani pa intaneti ndikulemba mawu akuti "Malawi Constitution" patsamba ili: https://malawilii.org/mw/consolidated_legislation/null kapena patsamba lililonse losakirapo zinthu.

Komanso kukhoza kuyanga'ana mlandu uliwonse omwe udaweruzikapo kale polemba dzina la mlanduwo pa tsamba losakirapo pa intenetipo ndipo mudzawupeza mlandu womwe mukufunawo.

# KODI MALAMULO AKULU NDI CHIYANI?



Mayiko ambiri padziko lapansi ali ndi Malamulo a Akulu oyendetsera mayiko awo. Malamulo a Akulu amakhala pamwamba pa lamulo lililonse mdzikolo. Lamulo lililonse lokhazikitsidwa mdzikomo komanso kayendetsedwe kaboma ndi ntchito za bomalo zimayenera kugwirizana ndi Malamulo a Akuluwo. Malamulo a Akuluwa amalongosola momwe boma liyenera kugwirira ntchito, za ufulu wachibadwidwe womwe anthu mdzikolo ali nawo, komanso momwe mabungwe aboma monga a Polisi, ayenera kugwirira ntchito.

Mayiko ambiri amalemba Malamulo a Akuluwa ngakhale kuti mayiko ena salemba malamulowa. M'mayiko omwe Malamulo a Akuluwa sadalembedwe, malamulowa amakhazikitsidwa ngati miyambo ndi machitidwe a chikhalidwe cha anthu yomwe ndi yofala kwambiri mdzikomo. Nthawi zambiri, Malamulo a Akulu amafotokoza bwino mtundu wa boma lomwe dzikolo likufuna kukhala nalo. Malamulowa amaululanso mavuto omwe dziko lidakumana nawo m'mbuyomu komanso ziyembekezo za fuko la dzikolo.




(CREDIT: judiciary.mw)

## Kulumikizana kwa ndale ndi malamulo a akulu oyendetsera dziko la malawi

M'mbuyomu dziko la Malawi lidali muulamuliro wa boma la nkhanza komanso lopondereza ufulu anthu kwambiri kufikira chaka cha 1994 pomwe dziko lino lidatuluka muulamuliro wa nkhanza wa chipani chimodzi. Mchaka cha 1994 chi, Malamulo a Akulu oyendetsera dziko adakonzedwanso. Mchikozedwechi Malamulowa adakhazikitsa ndondomeko zoteteza ufulu wa anthu kusiyana ndi momwe zinalili m'Malamulo a mchaka cha 1966. Malamulo atsopanowa adayala nsanamira za tsogolo lowala ndi ziyembekezo ndi zokhumbazi za a Malawi zomwe zimatumphuka m'mutu wachitatu, womwe umakamba za "Mfundo Zokhazikika" za Malamulo a Akuluwa. Izi zaumbidwa mkota motere:

- Munthu aliyense ayenera kugonjera malamulo;
- Amalawi ndiwomwe amapereka ulamuliro ndi maudindo aboma ndi ndale;
- Olamulira ndi adindo onse agwire ntchito yawo motsatira Malamulo oyendetsera dziko;
- Onse amene ali ndi udindo woyendetsa Boma alamulire motsata lamulo ndipo sayenera kugwiritsa ntchito mphamvu zawo molakwika;
- Mphamvu yoyendetsa boma ikhalepo ngati chikhulupiriro cha anthu pa Boma lawo chikupitirirabe, ndipo chikhulupirirochi chitha kupitirira ngati zinthu zikuchitika poyera, motsata zofuna za anthu popanda kuwabisira;
- Aliyense adababadwa ndi ulemu wake;
- Popeza aliyense adababadwa ndi ulemu wake, Boma ndi anthu onse azindikire ichi, ndi kuteteza ufulu wa chikhalirewu ndipo nkofunika kuteteza mokwana ufulu ndi zolankhulaza anthu onse masasamala kuti munthuyo angavote kapena ayi;
- Aliyense ndi wofanana pamaso pa malamulo;
- Aliyense ali ndi udindo kwa anthu ena, kwa mabanja lake, kudera lililonse, komanso kuboma. Izi zimafunika kuti anthu azilemekeza anzawo osati kuwasala ayi.

# MBIRI YA MALAMULO A AKULU ADZIKO LA MALAWI

Mchaka cha 1993, dziko la Malawi lidachita chisankho chadziko lonse chakumva maganizo a anthu pakayendetsedwe ka ndale; anthu adapatsidwa mpata wosankha pakati pa ulamuliro wachipani chimodzi ndi ulamuliro wa zipani zambiri. Ovota ambiri adasankha ulamuliro wa zipani zambiri. Zotsatira za chisankhochi zidaonetseratu kuti anthu amafuna chikonzedwe chakayendetsedwe ka boma. Mchikozodwemu mudali zinthu zingapo koma gawo loyambirira linali kukhazikitsa Malamulo a Akulu atsopano, ndipo izi zidachitika mchaka cha 1994.



(CREDIT: Parliment of Malawi)

Malamulo a Akulu oyendetsera dziko la Malawi a 1994 adalowa m'malo mwa Malamulo a Akulu omwe adakhazikitsidwa mchaka cha 1966. Nthawi ya chikozedwe cha Malamulo atsopanowa idali nthawi yofunika kwambiri m'mbiri ya dziko la Malawi. Malamulo atsopanowa adayala maziko a ufulu wa anthu aku Malawi ndi chimango cha boma lokomera anthu ambiri ndi losabisa kanthu kwa nzika zake, zomwe zidapatsidwa ufulu opereka maganizo awo pakayendetsedwe kake. Kabukuka kakufotokozerani ufulu womwe udalembedwa mu Mtolo wa Ufulu Wachibadwidwe m'Malamulo woyendetsera dziko a mchaka cha 1994 ndi momwe Malamulowa amatetezera ufulu wanu.

Anthu osiyanasiyana monga andale ochokera zipani zosiyanasiyana, akatswiri a za malamulo aku Malawi komanso mayiko akunja, oimira magulu amayi osiyanasiyana, ndi atsogoleri amitundu yosiyanasiyana womwe ndi omwe adagwira ntchito yokonzanso Malamulowa ndipo adakumana ndi kugwirizana kuti akhazikitse kaye Malamulo ongoyembekezera. Malamulo ongoyembekezerawa adakhazikitsa Mtolo wa Ufulu Wachibadwidwe wa anthu, womwe udaphatikizapo ufulu wokhala ndi moyo, ufulu wakusasalidwa, ufulu wokhala ndi moyo wa ulemu, ufulu wokasuma ku khothi ndi kuweruzidwa mwa mwachilungamo ndi makhothiwo, komanso ufulu wokhala ndi umunthu ndi kusazunzidwa kapena kupatsidwa chilango chakalavula gaga.

Vuto lomwe lidalipo pa Chikonzedwenso cha Malamulo a Akuluwa linali lakuti a Malawi ambiri sadatenge nawo gawo, sadafunsidwe ndipo sadapereke nawo maganizo awo pantchitoyi ngakhale panali anthu oyimirira magulu osiyanasiyana. Pa chifukwa ichi, nthumwi zomwe zimagwira ntchito ya chikonzedweyi zidagwirizana kuti Malamulo a Akukuluwa agwire ntchito mongoyembekezera kwa chaka chimodzi kuchokera mchaka cha 1994 kufikira chaka cha 1995. Ndipo mchaka cha 1995 Bungwe la Chikonzedweli lidaitanitsa msonkhano wina womwe cholinga chake chinali kufunsa maganizo anthumwi zosiyanasiyana pa Chikonzedwe cha Malamulochi. Msonkhano wowunikanso Malamulo oyendetsera dziko la Malawi udachitika ndipo kudabwera nthumwi zambiri zomwe zidazukuta Malamuluwa ndikusintha zina ndi zina m'Malamulowa. Mchaka cha 1995, Nyumba ya Malamulo yomwe idasankhidwa pa chisankho cha mchaka cha 1994 idavomereza Chikonzedwe cha Malamulochi mogwirizana ndi maganizo a msonkhano wa Chikozedwewu.

Mawu akalozera a m'Malamulo a Akuluwa amasonyeza khumbo la a Malawi pakayendetsedwe ka boma lawo. Mawu a kalozerawa ali motere:




## MAWU AKALOZERA ANTHU AMUNO M' MALAWI-

*Pozindikira* kuti moyo wa munthu ndiponso umodzi pakati pa anthu onse olengedwa ndi chinthu cha mtengo wa patali;

*Motsogozedwa* m'maganizo awo atadzisanthula komanso pofuna nzeru za iwo onse;

*Pofuna* kuti ubwino pa miyoyo ya anthu onse ndi chitukuko pa iwo zikhazikike, kuphatikiza mtima wakuti ife ndife a Malawi ndipo pafunika mtendere pakati pa mayiko;

*Pofunitsitsa* kuti tikhazikitse maziko a Malamulo okhozikika oyendetsera Boma la Malawi lochita zinthu poyera, lotumikira olamulidwa ndi losabisira anthu;

PANO tikukhazikitsa Malamulo awa oyendetsera Dziko la Malawi.

## Chikonzedwe cha Malamulo a Akulu mchaka cha 1994

Zaka za ma 1990 ndi zaka za chikonzedwe ya ufulu wa anthu ku Malawi. Chikonzedwechi chidachepetsa mphamvu za boma zomwe zidathandiza kuteteza ufulu wa anthu mdziko la Malawi. Chikonzedwechi chidathetsa ulamuliro wa nkhanza ndi kuika nsanamira zoteteza ufulu wa anthu osiyasiyana ndi kubweretsa boma lokomera anthu onse kusiyana ndi ulamuliro wakale. Malinga ndi Malamulo a Mchikozedwechi, aliyense ndi wotetezedwa, ndipo boma silingachitire anthu ake nkhanza kapena kuwaphwanyira ufulu wawo popeza Bomalo nalonso limayenera kogonjera Malamulowa.



(CREDIT: ICRISAT)

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO : BOMA LOGONJERA MALAMULO

**(Kulondoloza boma pamene lagwiritsa ntchito mphamvu yake molakwika)**

Malamulo a Akulu oyendetsera dziko la Malawi amapereka ufulu kwa anthu kuzenga mlandu boma ngati bomalo laphwanya ufulu wa anthuwo zomwe zinali zosatheka muulamuliro wa chipani chimodzi.

Chigamulo cha Mlandu wa a *MM ndi anzawo ena ndi Boma* ndi chitsanzo chabwino cha momwe anthu amatha kusumira boma ku Malawi kuno. Mchaka cha 2019, amayi ndi atsikana ambiri kwa Msundwe ku Lilongwe adagwiririidwa, kugwiridwa ku maliseche, kumenyedwa komanso kuchitiridwa nkhanza zosiyanasiyana ndi a Polisi mkatikati mwa ziwawa zomwe zimachitika pomwe anthu sadakhutire ndi zotsatira za chisankho cha mchaka cha 2019. A Polisiwa adachita nkhanza zonsezi pofuna kubwezera kuphedwa kwa wa Polisi mnzawo. Apolisi sadafufuze za nkhaniyi kapena kumanga a Polisi anzawo omwe adachitira chipongwe amayi ndi atsikanawa. Palibe wa Polisi yemwe adamangidwa kapena kuzengedwa mlandu pa nkhaniyi ngakhale amayi ndi atsikanawa adakadandaula ku Polisi. A Polisi sadafufunze mokwanira nkhaniyi.

Amayi ndi atsikana 18 mwa ochitiridwa nkhanzawa adakasumira a Polisi ku Khothi kuti mwa zina apepesedwe pa nkhanza zomwe adawachitirazo. Pogamula mlanduwo, Khothilo la Likulu lidati nkhanza zotere zidawaphwanyira amayi ndi atsikanawa ufulu wawo wachibadwidwe. Bwalo lidapeza kuti Boma lidalephera udindo wake woteteza ufulu wa odandaula pa mlanduwu ku nkhanza zomwe a Polisi wa adawachitira. Bwalo lidagamulanso kuti nthambi ya a Polisi idaphwanyanso ufulu wa ozunzidwawa polephera kufufuza za nkhaniyi, posayang'anira wogwira ntchito awo, komanso osapereka chipepeso kwa amayi ndi atsikanawa. Bwalo lidaunikiranso kuti nkhanzazi zidaipitsitsa popeza kuti zidachitidwa ndi nthambi ya boma yomwe imayenera kuteteza anthu osati kuwazunza ndipo pa chifukwachi boma limayenera kuimbidwadi mlandu. Chigamulochi chidati a Polisi adalephera kukwaniritsa udindo wawo malinga ndi Malamulo, pozunza ndi kuchitira nkhanza zosiyanasiyana amayi ndi atsikanawo. Ndipo Khothilo lidapitirira kunena kuti Malamulo oyendetsera dziko lino amapereka udindo ku boma ndipo "ufulu wofotokozedwa mugawo la mtolo wa ufulu wa chibadwidwe wa m'Malamulo a Akuluwa zizilemekezedwa ndi kukwezedwa ndi Mtsogoleri wadziko, nyumba ya Malamulo, makhothi komanso mabungwe onse a boma ndi nthambi zake." Malamulo oyendetsera dziko lino adaperekanso udindo kwa a Polisi kupereka chitetezo cha anthu komanso ufulu wa anthu m'Malawi."

Mlanduwu ukutipatsa chitsanzo chabwino cha momwe anthu wamba angagwiritsire ntchito Malamulo a Akuluwa posumira boma. Kuchokera pa mlanduwu, titha kuwona momwe anthu angazengere boma mlandu pa zomwe likuchita ndi kupewa kuphwanya ufulu mtsogolo.

# ZAMKATI MWA M'MALAMULO A AKULUWA

Malamulo a Akulu oyendetsera dziko la Malawi ndi malamulo a akulu kwambiri mdziko muno ndipo ali pamwamba pa aliyense mdziko muno kuphatikiza boma ndi aliyense woimira boma ndi mtsogoleri wa Mtsogoleri wa Dziko. Aliyense, mosasamala za kulemera kwake, kapena mphamvu yake, akuyenera kugonjera Malamulo ndipo ayenera kulemekeza ufulu wa ena. Malamulo a Akuluwa amati:

*"Mabungwe ndi anthu onse agwiritse ntchito ndi kulemekeza Malamulo ano ndikuopa mphamvu za lamulo, palibe bungwe kapena munthu uyo angapambane mphamvu za lamulo."*

Malamulo a Akuluwa ali ndi mitu 23. Mutu uliwonse umafotokoza Mfundo zosiyanasiyana za kayendetsedwe ka boma.


## NDONDOMEKO YA MITU YA MALAMULO A AKULU OYENDETSERA DZIKO LA MALAWI

- Mawu a Kalozera
- Mutu 1: Dziko la Malawi
- Mutu 2: Kugwiritsidwe ntchito ndi kamasulidwe
- Mutu 3: Mfundo zokhazikiza
- Mutu 4: Ufulu wa anthu
- Mutu 5: Zokhudza nzika
- Mutu 6: Gawo la Boma Lopanga Malamulo
- Mutu 7: Chisankho
- Mutu 8: Gawo la Mutu wa Boma
- Mutu 9: Gawo la Oweruza
- Mutu 10: Ombudzimani
- Mutu 11: Bungwe Loteteza Ufulu wa anthu
- Mutu 12: Bungwe Loona Chilongosoko cha Malamulo
- Mutu 13: Bwalo Loona za Chipepeso
- Mutu 14: Maboma a ang'ono
- Mutu 15: A Polisi
- Mutu 16: Gulu la nkhondo
- Mutu 17: Ndende za Boma
- Mutu 18: Za chuma
- Mutu 19: Banki yaikulu ya Boma la Malawi
- Mutu 20: Ogwira ntchito zaboma
- Mutu 21: Kasinthidwe ka Malamulo oyendetsera boma
- Mutu 22: Zina ndi zina malingana ndi kusinthaku
- Gawo 23: Zina


Monga momwe mukuonera mitu yosiyanasiyana ya Malamulo a Akuluwa, imaongolera ntchito zosiyanasiyana za boma la Malawi.

# MGAWIKANO WA NTCHITO NDI MPHAMVU WA NTHAMBI ZITATU ZABOMA

Malamulo a Akulu a dziko la Malawi adakonzedwa moti dziko lino lipewe mavuto omwe mayiko amakumana nawo nthawi zambiri ngati mphamvu zoyendetsera boma zili m’manja  mwa munthu m'modzi kapena bungwe limodzi. Mphamvu zoyendetsera dziko zikasefukira mwa Mtsogoleri wa Dziko kumakhala kosavuta kuti Mtsogoleriyo ndi boma lake azipondereza anthu ndi kuwachitira nkhanza. Popewa zimenezi Malamulo a Akuluwa adagawa ntchito ndi mphamvu za boma pakati pa nthambi zitatu zosiyana ndi cholinga chakuti nthambizi ziziwongolerana kuti pasapezeke nthambi yogwiritsa ntchito mphamvu yake molakwika. Malamulowa adakhazikitsa nthambi za Boma zitatu zosiyana izi:



**Nthambi yopanga Malamulo:** M’nthambiyi muli nyumba yamalamulo, imapanga malamulowo



**Nthambi ya Mutu wa Boma:** Nthambi iyi imapangidwa ndi Mtsogoleri wadziko, Wachiwiri wake ndi nduna zake zonse. Iyoyi imakhazikitsa malamulo ndi ndondomeko zaboma ndikuzigwiritsa ntchito ndi kuzikwaniritsa



**Nthambi ya Makhothi:** Nthambi iyi muli makhothi ndi oweruza milandu osiyanasiyana omweamweruza milandu ndi kutanthauzira malamulo

Ntchito ndi mphamvu zomwe nthambi zitatuzi zili nazo zidakhazikitsidwa m’Malamulo a Akulu, pa gawo 7, 8 ndi 9. Nthambi iliyonse ya boma ndi yodziimira payokha ndipo palibe yofunika kwambiri kuposa inzake. Nthambizi zimaongolererana ina ndi inzake zomwe zimathandiza kuti nthambi zonsezi zizitsata Malamulowa kupewa kuti atsogoleri anthambizi angamagwiritse ntchito mphamvu zawo molakwika. Mgawikano wa mphamvu ndi ulamuliro wa Nthambi zitatuzi ndi wofunika kwambiri poteteza ufulu wachibadwidwe wa anthu. Monga tionere mu zitsanzo zathu, nthawi zambiri pali kufunika kwakuti atsogoleri aziyendetsa boma mogonjera Malamulowa.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO

### Mgawikano wa Ntchito ndi Mphamvu wa Nthambi Zitatu za boma ndi kuwongolerana kwawo

Mayiko ambiri pa dziko lonse lapansi adakhazikitsa ndondomeko zosiyanasiyana zolimbina ndi mulili wa COVID-19 kuphatikizapo m'bindikiro wa anthu. Malawi linali limodzi mwa mayiko oterewa. Boma la Malawi lili ndi udindo owonetsetsa kuti ndondomeko za m'bindikirozi zikhale zovomerezeka ndi Malamulo a Akulu ngakhale kuti likulimbana ndi matenda adzidzidzi owopseza umoyo wa anthu. Chigamulo cha Khothi la Likulu pa mlandu wa a *Kathumba ndi Ena wolimbana ndi Mtsogoleri wadziko la Malawi*, pa mlandu omwe odandaula amafuna kuti Khoti liunike ngati malamulo a m'bindikiro omwe nduna ya za umoyo adakhazikitsa motsatira Malamulo a Akulu mwazina, ngati kakonzedwe ka malamulowo sikadaphwanye mgawanikano wa ntchito ndi mphamvu pakati pa nthambi zitatu za boma.

Khothi la Likulu lidapeza kuti Mutu wa Boma la Malawi udapereka malamulo a m'bindikiro kudzera ku mwanduna ya za umoyo mwayokha osafunsa Nyumba ya Malamulo monga momwe Malamulo amanenera. Malamulo amafotokoza momveka bwino kuti 'Nyumba ya Malamulo yokha ndi yomwe imapanga Malamulo,' ndipo, ndi chifukwa chake kunali kuphwanya Malamulo a mgawikano wa ntchito ndi mphamvu pa kati pa Mutu wa Boma ndi Nyumba ya Malamulo kuti Nduna ya za umoyo idapanga lamulo la m'bindikiro payokha. M'lamulo la m'bindikiroli Nduna ya za umuyoyi idalamulanso kuti makhothi atsekedwe ngakhale kuti amene ali ndi mphamvu yolamula izi ndi Mkulu wa makhothi osati Nduna ya Boma. Khothi lidalamula kuti malamulo a m'bindikirowo anali osafikira ndi ovomerezeka pa mulingo ma Malamulo a Akulu udaika ndipo kotero anali osavomerezeka mu ulamuliro wa demokalase.

Chigamulochi chidatsindika kuti mgawikano wa ntchito ndi mphamvu pakati pa nthambi zitatu zaboma umateteza ufulu wa anthu wachibadwidwe popeza nthambizi zimabwezana ndi kuwongolererana ngati nthambi ina ikumphwanya malamulo. Khothi lidaunikira kuti nyumba ya malamulo ndi makhothi ali ndi gawo lofunikira powonetsetsa kuti Malamulo a Akuluwa akutsatidwa ndi kuwonetsetsanso kuti boma likumvera maganizo a aMalawi pakayendetsedwe kake ndipo milili wa Covid 19 sichifukwa chokwanira chophwanyira Malamulowa.

# MNDANDANDA MAKHOTHI KU MALAWI

Ku Malawi kuli mabwalo a makhothi osiyanasiyana omwe alinso ndi magawo osiyanasiyana omwe amaweruza milandu ya mitindumitundu. Makhothi onsewa amagwira ntchito limodzi poweruza milandu mosakondera ndi mwachangu.

Malamulo a Akuluwa amapereka udindo womwe Woweruza aliyense amayenera kutsatira poweruza milandu monga uwu:

- Kukhala odziyimira pawokha komanso osakondera
- Kutanthauzira ndi kugwiritsa ntchito lamulo
- Kulimbikitsa ndi kuteteza malamulo, demokalase, ndi ufulu wa anthu wa chibadwidwe

Pali mitundu itatu ya makhothi ku Malawi:

**Khothi La Likulu Kwambiri la apilo** (Supreme Court of Appeal)- ili ndi khothi la Likulu kwambiri ku Malawi, ndipo limamva apilo ya milandu yochokera ku Khothi la Likulu ndi mabungwe ena oweruza nkhani. Aliyense amatha kupanga apilo ku Khothili ngati sanakhutire ndi chigamulo cha Khothi la Likulu. Pali Khothi La Likulu la Apilo limodzi lokha, ndipo lili ku Blantyre.

**Khothi La Likulu la Malawi** – Khothi la Likulu limazenga mlandu uliwonse waupandu ndi wapachiweniweni omwe, ndipo litha kuwunikanso malamulo womwe apangidwa komanso kayendetsedwe ka boma pofuna kuunika ngati malamulo ndi zochita zonse za boma zikugwirizana ndi Malamulo a Akulu. Khothili lili ndi magawo osiyanasiyana – Gawo la Milandu ya pa Chiweniweni (Civil Division), Gawo la Milandu ya za Malonda (Commercial Division), Gawo la Milandu ya Upandu (Criminal Division), Gawo la Milandu ya pa Banja ndi Chuma cha Masiye (Family and Probate Division) ndi Gawo la Milandu ya Misonkho (Revenue Division). Makhothi a akuluwa ali m’mizinda yonse ya mdziko lino.

**Makhothi a Ang’ono** - pali mitundu inayi ya makhothi a ang'onoang'ono: Khothi Loona Milandu ya ku Ntchito – uku ndi kumene milandu ya pantchito imazengedwa; Makhoti a Majisitireti, lomwe limazenga milandu ya ing’ono ya upandu ndi ya pa chiweniweni; Khothi la Ana, lomwe limazenga milandu ya ana ya upandu ndi ya chiweniweni yomwe; Makhothi am'midzi, omwe adapangidwa kuti athandize anthu kupeza chilungamo mosavuta. Mabwalo am’midziwa adakhazikitsidwa ndi lamulo la makhoti akumidzi ndipo amapezeka m'maboma onse 27 ku Malawi kuno. Ntchito yokhazikitsa makhothi ena am'derawa ikadali mkati pano.

# Khothi Lalikulu la Apilo – Supreme Court of Appeal

Ngati mulandu ndi wokhudza kuphwanyidwa kwa ufulu wa anthu, ndipo wodandaula sadakhutitsidwe ndipo akuganiza kuti sadalandire chilungamo, atha kupita ku Khothi Loona za Ufulu wa Anthu ku Africa (African Court of Human and People's Rights) lomwe lili mdziko la Tanzania.

Ngati mulandu waweruzidwa ku Khothi Lalikulu (High Court), ukhoza kukadandaulidwansa ku Khothi Lalikulu la Apilo (Supreme Court of Appeal).

## Khothi Lalikulu la Malawi

Gawo la Milandu ya pa Chiweniweni
Gawo la Milandu ya za Malonda
Gawo la Milandu ya Upandu
Gawo la Milandu ya Banja ndi Chuma cha Masiye
Gawo la Milandu ya Misonkho



Ngati mulandu waweruzidwa ku Khothi Laling'ono (Subordinate Court), utha kukadandaulidwanso ku Khothi Lalikulu (High Court)

## Makhothi ang'onoang'ono

Makhothi a Magesitileti
Khothi la za Ntchito
Khothi la Chilungamo cha Ana
Makhothi a M'maboma aang'ono

Mikanagano yambiri imaweruzidwa koyamba ku Makhothi ang'onoang'ono (Subordinate Courts). Makhothi awa ndi osavuta kuwafikira kapena kuwapeza ndiponso ndi otchipa. Mikangano ina imatha kuyamba kuweruzidwa ku Khothi Lalikulu (High Court)

Kuphatikiza pa makhothi akuno ku Malawi, palinso khothi lina lomwe anthu aku Malawi angakasume ngati akuganiza kuti ufulu wawo waphwanyidwa ndipo sanakhutire ndi momwe makhothi akuno ku Malawi aweruzira mlanduwo. Khothili limatchedwa Khothi Loona za Ufulu wa Chibadwidwe wa Anthu mu Africa (African Court on Human and People's Rights) lomwe lili mu mzinda wa Arusha mdziko la Tanzania. Malawi ndi limodzi mwa mayiko ochepa omwe amalola anthu ndi mabungwe kukalimang'alira ku khothili.

# MAZIKO A UFULU WACHIBADWIDWE

Ufulu wa chibadwidwe wa munthu aliyense ndi imodzi mwa nsanamira za Malamulo a AKulu oyendetsera dziko la Malawi. Ufulu wa chibadwidwewu udalembedwa mu Mtolo wa ufulu wachibadwidwe m'mutu 4 ya Malamulo a Akuluwa.

## Ufulu ndi chiyani?

Ufulu ndi zilonjerero ndi ziyenerezo zomwe munthu aliyense amapatsidwa ndi malamulo – kapena kuti chinthu chomwe munthu angakakamize boma kuti limuchitire. Mwachitsanzo munthu akhoza kukhala ndi ufulu wosunga zinsinsi zomwe ngakhale boma silingaloledwe kuziona. Munthu alinso ndi ufulu wolandira thandizo la ku chipatala.

**CHITSANZO**

Ufulu wachibadwidwe ukhoza kukhala chinthu chomwe boma limayenera kukuchirani:

"Ndili ndi ufulu woweruzidwa mlandu mwachilungamo"

Ngati wina ali ndi ufulu kuweruzidwa mlandu mwachilungamo, boma limayenera kupereka kapena kukonza zinthu zonse zomwe zimapangitsa kuti mlanduwo uweruzidwe mwachilungamo, ufuluwu umawonjezera ufulu wotengedwa kuti munthuyo ndi wosalakwa ngati khothi silinamupeze olakwa, ufulu wa munthuo wozengedwa mlandu wosaperekera umboni pa mlandu wake, ufulu woweruzidwa mwachangu komanso ufulu oimiriridwa ndi loya pa mlanduwo. Boma lili ndi udindo wopereka zinthu zofunikira kuti munthu ozedwedwa mlandu aweruzidwe mwachilungamo.

Palinso ufulu wina wachibadwidwe omwe boma limafunika kuchita kanthu kena:

"Ndili ndi ufulu wosazunzidwa"

Boma silingazunze aliyense, ndipo liyenera kuwonetsetsa kuti palibe yemwe akuzunza mnzake mdzikomo.



(CREDIT: Commonwealth Secretariat)


Dziko la Malawi laonetsa kudzipereka kwakukulu popititsa patsogolo ufulu wa anthu polemba ufulu wa chibadwidwe m'Malamulo a Akulu. Ufulu wachibadwidwewu ndi chida chomwe anthu mdziko muno amadziteteza nacho ku nkhanza zomwe boma komanso anthu anzawo angawachitire.

## Kulukanalukana kwa ufulu wa chibadwidwe

Mumtolo wa ufulu wachibadwidwe muli ufulu osiyanasiyana monga ufulu wokhala ndi moyo, ufulu wa chinsinsi, ufulu woyankhula za kukhosi. Palibe ufulu womwe ndi wofunika kwambiri kuposa unzake. Ufulu uliwonse umamangirirana ndi unzake ndikupanga mtolo wopangitsa kuti anthu azikhala ndi moyo wabwino.

Ufulu wa chibadwidwe wosiyanasiyana umaluka mtolo womwe umathandiza kuti ufulu uliwonse ukhale ndi tanthauzo. Ufulu omwe ali mu Mtolo wa Ufulu wachibadwidwe udayala maziko a moyo wokoma ndi ulemu zomwe ndi zothandiza kupititsa patsogolo miyoyo ya anthu.

## Momwe mungamenyerere ufulu wanu wachibadwidwe




Ufulu wa chibadwidwe udaikidwa m'Malamulo a Akulu kuti anthu azimenyera ufulu wawo mosavuta pamene achitilidwa nkhanza.

Malamulo a Akulu adaika njira zingapo zomenyera ufulu. Njira yomwe imagwiritsidwa ntchito kwambiri ndi kukasuma ku Khothi. Makhothi akhoza kulamula boma kuti likonze zinthu zomwe zaphwanya ufulu wa chibadwidwe. Machitsanzo Khothi likhoza kulamula kuti boma lilipire chipuputa misozi kapena kuletsa zophwanya ufulu wa chibadwidwe.

Palinso mabungwe ena omwe amathandiza anthu omwe ufulu wawo waphwanyidwa ngakhale kuti nthawi zambiri makhothi ndi omwe amateteza ufulu wa chibadwidwe wa anthu. Pali mabungwe angapo omwe adakhazikitsidwa ndi Malamulo a Akulu, monga **Bungwe Loteteza Ufulu wa Anthu, (Malawi Human Rights Commission) komanso Ombudzimani.** Mabungwewa adakhazikitsidwa kuti azithandiza anthu omwe ufulu wawo waphwanyidwa - mwachitsanzo, Bungwe Loteteza Ufulu wa Anthu limafufuza madandaulo a zakuphwanyidwa kwa ufulu, ndipo lili ndi mphamvu zingapo zomwe limagwiritsa ntchito pothetsera mchitidwe wophwanyirana ufuluwu. Munthu aliyense payekha kapena gulu la anthu atha kukamang'ara ku Bungwe Loteteza Ufulu wa Anthu ngati akuganiza kuti ufulu wawo ukuphwanyidwa.



Palinso mabungwe ena omwe si aboma omwe amathandiza kumenyera ufulu wa anthu. Mabungwewa nthawi zambiri amagwirira ntchito limodzi ndi Boma poteteza ufulu wa anthu ku Malawi, ndipo pamene ufulu waphwanyidwa amatengera milandu kukhothi kapena kuyanjanitsa odandaula ndi odandaulidwa asanapite ku khothi.

## Kuimitsidwa Ufulu wa chibadwidwe

Boma lili ndi mphamvu zoimitsa ufulu wachibadwidwe wa anthu. Kuimitsa ufuluku sikuyenera kuchitika mwachisawawa ndipo mphamvuzi zimagwiritsidwa ntchito m'nthawi ya nkhondo kapena ya ngozi za dzidzidzi. Mwachitsanzo, ufulu wochita zionetsero ukhoza kuimitsidwa ngati chitetezo chili chosakwanira kapena kukuchitika nkhondo. Izi ndi zina mwazifukwa zokwanira zoimitsira ufulu wochita zionetsero.

Muliri wa COVID-19 womwe umafala kwambiri ukutipatsa zitsanzo zambiri za momwe ufulu wa chibadwidwe ungasokonekerere. Mwachitsanzo, COVID-19 itabwera kumene, anthu amakanika kusonkhana kapena kuyenda momasuka poopa mliriwu.  Malamulo okhudza muliriwu adaletsa anthu opitilira 250 kusonkhana pamodzi. Ufulu umaimitsidwa chonchi pakakhala kuti kuimitsako nkofunika polimbana ndi vuto lomwe dziko lakumana nalo ndipo boma silingachitire mwina koma kuimitsa ufuluwo.

Chigamulo cha Khothi la Likulu pa mlandu wa a *Kathumba ndi Ena wolimbana ndi Mtsogoleri wadziko la Malawi*, omwe taufotokoza kale udaunikira momveka kuti payenera kukhala zifukwa zokwanira ndi zovomerezeka ndi Malamulo a Akulu kuti Boma liimitse kaye ufulu wa chibadwidwe wa anthu.



# MTOLO WA UFULU WACHIBADWIDWE

Mtolo wa ufulu wachibadwidwe omwe uli m'Malamulo a Akulu umafotokoza za ufulu omwe aliyense ali nawo, umafotokozaanso za momwe aliyense angamenyerere ufuluwo, komanso momwe Boma lingaimitsire ufuluwo. Ufuluwu ndi wotetezedwa kwambiri chifukwa chakuti Bomanso nalo limayenera kugonjera Malamulo a Akuluwa omwe amateteza ufuluwu.

## Chifukwa chomwe dziko la Malawi limateteza ufulu wa chibadwidwe wa anthu

Mtolo wa ufulu wachibadwidwe umatiuza chifukwa chomwe dziko la Malawi limatetezera ufulu wa chibadwidwe: "popeza kuti munthu aliyense adadabwa ndi ulemu wake, Boma ndi anthu onse azindikire ichi ndi kuteteza ufulu wachibadwidwewu." Ufulu wa chibadwidwewu udalembedwa m'Malamulo a Akuluwa chifukwa ndi wofunika kwambiri kwa anthu- sudapangidwe ndi malamulo aliwonse ayi koma umatetezedwa ndi Malamulo a Akuluwo zomwe zimathandiza anthu kuti azimenyerera ufuluwu mosavuta. Malamulo a Akuluwa amafotokozanso kuti ufulu wa chibadwidwe ndi "njira imodzi yotukulira miyoyo ya a Malawi."

Malamulo a Akuluwa adayala maziko oyendetsera dziko lino ndipo amalimbikitsa dziko la Malawi kuti likhazikike pa ulamuliro wogonjera malamulo ndi wokomera anthu onse womwe zimapangitsa kuti ufulu wachibadwidwe wa anthu onse utetezedwe ndi kupita patsogolo.

## Tanthauzo la ufulu chibadwidwe kwa inu

Pali ufulu osiyanasiyana omwe umamanga mtolo wa ufulu wa chibadwidwe. Ufuluwu udakhazikitsidwa ndi cholinga choteteza ulemu wa anthu. Ufulu wina umafunika kuti Boma litengepo mbali lowukwiniritsa pothandiza anthu ndipo wina umafunika kuti Boma lisalowerere pa miyoyo ya anthu.



(CREDIT: Rob McConaghy)

# MNDANDANDA WA MTOLO WA UFULU WACHIBADWIDWE

16 - Ufulu woakhala ndi moyo
17 - Ufulu wosaphedwa mwasiwawa
18 - Ufulu wa ufulu womasuka
19 - Ufulu wokhala mwa umunthu
20 - Ufulu wosasalidwa
21 - Ufulu wokhala ndi chinsinsi
22 – Ufulu woteteza banja, kuphatikiza ufulu wa aliyense:-

- m'banjamo kutetezedwa wolemekedwa;
- Palibe amene angakakamizike kukwatira

23 - Ufulu wa ana
24 - Ufulu wa amayi, kuphatikiza ufulu:-

- wotetezedwa mofanana ndi ulemu
- kukhala ndi katundu, mwaiye yekha kapena ndi anzake;
- kukhala ndi ana ake komanso ufulu wolera anawo momwe angafunire;
- wogawana katundu mwachilungamo pakutha kwa ukwati;
- wakuti boma likhazikitse malamulo woteteza amayi ku nkhanza;
- kukuzunzidwa, kusalidwa, komanso kuteteza ku kulandidwa katundu

25 - Ufulu wamaphunziro
26 -Ufulu wogwiritsa ntchito chilankhulo komanso kutenga nawo mbali pachikhalidwe chamtundu mwachifuniro chake
27 - Ufulu womasulidwa ku ukapolo kapena ku kupsinjika
28 - Ufulu wopeza katundu kapena chuma ndiponso kusalandidwa chumacho

29 - Ufulu wodzipezera zofuna za moyo wake
30 - Ufulu pa chuma, pa khalidwe ndi pa ndale makamaka amayi, ana, ndi anthu omwe ali ndi ulumali
31 - Ufulu wogwirira ntchito mwachilungamo ndi kulipidwa moyenera
32 - Ufulu wolowa nawo m'bungwe lililonse
33 - Ufulu wokhala ndi maganizo ake, chipembedzo chake chikumbumtima, ndi chikhulupiriro chake, zolingalira komanso nzeru za maphunziro
34 - Ufulu woganiza
35 - Ufulu wolankhula za kukhosi
36 - Ufulu wa atolankhani
37 – Ufulu wopeza nkhani
38 - Ufulu wosonkhana ndi anzake ndi kuchita ziwonetsero
39 - Ufulu woyenda ndi kukhala kulikonse m'Malawi
40 - Ufulu wotenga nawo mbali pandale
41 – Ufulu wokasuma kukhothi
42 - Ufulu wa omangidwa, akaidi, ndi kuweruzidwa mwachilungamo
43 – Ufulu wothandizidwa mwachulungamo



# KUTAMBASULA MTOLO WA UFULU WACHIBADWIDWE MWACHIDULE

Tsopano tiona ufulu womwe uli mu Mtolo wa Ufulu wachibadwidwe m'Malamulo a Akulu oyendetsera Boma la Malawi mwachidule. Muthakuwerenga tsatanetsane wa Mtolo wa Ufuluwu m'gawo 4 la Malamulo a Akuluwa.

## Gawo 4 - Ufulu wa anthu

15 - **Nthambi zonse za boma** – Mutu wa Boma, Nyumba ya Malamulo, ndi Yoweluza milandu, ndiponso munthu aliyense ku Malawi kuno akuyenera kulemekeza ufulu womwe uli mu Mtolo wa ufulu wachibadwidwe. Munthu aliyense ndi bungwe lililonse mdziko la Malawi lingathe kupita ku khothi kukamenyera ufuluwo womwe wphwanyidwa kuti awonetsetse kuti ufuluwo watetezedwa. Alinso ndi ufulu wokadandaula kwa Ombudzimani, Bungwe Loteteza Ufulu wa Anthu kapena bungwe lina lililonse la boma.

16 - **Moyo** - Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi moyo ndipo wina aliyense saloledwa kuononga moyo wa nzake mwadala popanda chifukwa chokwanira (ngati kupha munthu mudziteteza.)

### CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: ALIYENSE ALI NDI UFULU WOKHALA NDI MOYO

**Ufulu wamoyo ukuyenera kutetezedwa, kupanda kutero munthu sangakhale ndi ufulu uliwonse**

Mchaka cha 2021, Khothi la Likulu la Apilo lidaweruza mlandu wa *Khoviwa ndi Boma* ndipo m'modzi wa Woweruza ku Khothilo adagamula kuti chilango chonyonga munthu chimaphwanya Malamulo a Akulu pophwanya ufulu wa munthu wokhala ndi moyo. Woweruzayo adati "ufulu wokhala ndi moyo ndiye manthu waufulu uliwonse. Popanda ufulu wokhala ndi moyo, ufulu wina uliwonse sungakhalepo. Chilango chonyonga munthu chimaduliratu muzu wa ufulu wokhala ndi moyo."

Woweruzayo adalamula kuti chilango chonyonga anthu ncholetsedwa kuno ku Malawi kamba kakuti ndi chophwanya ufulu wa chibadwidwe wa munthu wonyongedwawo. Komabe, Oweruza anzawo mzigamulo zawo adatsutana nawo zomwe zikutanthauza kuti Khothi La Likulu la Apilo silidathetse chilango chonyonga anthu ku Malawi kuno. Komabe, anthu ena ali ndi chiyembekezo kuti mtsogolomu chilango chonyonga anthu chidzathetsedwa mdziko muno.

Khothi La Likulu lidayenera kulingalira mozana zomwe Malamulo a Akulu amanena pa za chilango chonyongedwa ngakhale anthu ambiri ku Malawi amagwirizana ndi chilango chonyongedwachi. Khothi liyenera kutsatira Malamulo osati maganizo a anthu popereka chigamulo pa chilango chonyongedwachi kuti liteteze bwino ufulu wa anthu ovutika.

17 – **Kupha anthu mwachipulula** – Kupha anthu mwachipulula ndi kupha gulu la anthu chifukwa cha mtundu wawo ndipo nkoletsedwa muno m'Malawi ndipo boma liyenera kulanga onse ochita izi.

18 - **Kumasuka** – Munthu aliyense ali ndi ufulu okhala momasuka zomwe zimaletsa kumangidwa mwachisawawa kapena kupanga ziganizo zokhudza moyo wake.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO : UFULU WOMASUKA

### A Polisi asamange anthu mwasawawa

Chigamulo cha mlandu wa m'chaka cha 2016 wa pakati pa *Boma ndi Pempho Banda*, Khothi La Likulu ligamula kuti anthu ali ndi ufulu osamamangidwa mwachisawawa ndipo azimangidwa pokakhala chifukwa chokwanitra basi. A Polisi adamanga amayi 19 powaganizira kuti amachita uhule ngakhale padalibe umboni wotsimikiza nkhaniyi. A Polisi adamanga anthuwa kamba kowakaikira chabe. Chigamulochi chikutsimimiza kuti kumangidwa mwachisawawa ndi kupha ufulu womasuka ndipo ndi koletsedwa ndi Malamulo a Akulu ndipo a Polisi ayenera kukhala ndi zifukwa zokwanira zomangira munthu.

19 – **Ufulu wa umunthu** - Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi umunthu wake womwe uyenera kulemekedwa ndi anthu anzake komanso boma. Ufuluwu umakhala ndi munthu aliyense ngakhale amene wamangidwa kapena yemwe akugwira ukaidi. Munthu asasunguzidwe mnjira iliyonse kapena kupatsidwa chilango chomuzunza kapena kumuyalutsa. Palibe munthu yemwe amayenera kuchotseredwa ulemu wake kapena kuchitidwa nkhanza iliyonse. Ufulu wa umuthu umaletsa achipatala komanso asayansi kuchita kufukufuku ndi thupi la munthu opanda chilolezo chamwini thupiyo.




## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WA UMUNTHU

### Ufulu wa ulemu umateteza anthu ku nkhanza za boma

Chigamulo cha Mlandu wa a *MM ndi anzawo ena ndi Boma* womwe wakambidwa koyambirira kwa kabukuka, a Polisi adayalutsa amayi powagwiririra ndi kuwagwira maliseche. Ufulu wa umunthu umaletsa kuti munthu aliyense achitidwe nkhanza ngati momwe zidawachitikira amayi ndi atsikanawa. Khothi lidagamula kuti a Polisi adawaphwanyira ufulu amayi ndi atsikanawa posafufuza zachipongwechi ndi posamanga ndi kuzenga mlandu a Polisi omwe adachita izi. Ufulu wa umunthu umaletsa kuti nkhanza ngati izi zichitikire munthu aliyense monga mowe zidawachtikirira amayiwa.

20 – **Ufulu wasasalidwa** – Sikuloledwa kumusala munthu mwamtundu uliwonse, ndipo Malamulo adzateteza onse mokwana popanda tsankho chifukwa cha mtundu, khungu, chifukwa chakuti ndi wamwamuna kapena wamkazi, kapena chifukwa cha chilankhulo, chipembedzo, maganizo ake pankhani ya ndale kapena nkhani zina, kapena kuti ndi m'Malawi kapena ayi, kapena chifukwa chakomwe amachokera, kulumala, chuma, chibadwidwe kaya umo amonekera pakati a anzake.




## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WA UMUNTHU

### Munthu aliyense asasalidwe popanda chifukwa chomveka chovomerezedwa ndi lamulo

Mchaka cha 2008, pa mlandu wapakati pa *Banda ndi Lekha*, khothi lowereza milandu ya pa ntchito lidagamula mlandu wa munthu yemwe adachotsedwa ntchito chifukwa chopezeka ndi kachilombo koyambitsa matenda a Edzi ka HIV. Mchigamulo chake Khothi lidati kuchotsa munthu ntchito kamba kakuti ali ndi HIV ndi kuphwanya ufulu wa munthu osasalidwa zomwe zikutsutsana ndi Gawo 20 la Malamulo a Akulu. Izi zikutanthauza kuti Malamulo amateteza anthu omwe ali ndi kachilombo ka HIV ku tsankho lililonse.

21 - **Chinsinsi** – Munthu aliyense azikhala ndi zinsinsi zake, ndipo mwaizo zitanthauzidwe kuti sikuloledwa kumuchita chipikisheni mthupi lake, kunyumba kwake, kumutengera katundu kapena kuwerenga umakalata ake kapena m'mafoni ake ndi uthenga wake uli onse.

22 - **Banja ndi Ukwati** - Mabanja akuyenera kutetezedwa ndi boma. Munthu aliyense m'banja azilemekezekedwa ndi kutetezedwa ku nkhanza ndi kuchipsinjo chilichonse. Amuna ndi akazi onse ali ndi ufulu wolowa m'baanja kapena wokwatira kapena kukwatiwa mwakufuna kwawo. Munthu wobzola zaka 18 zakubadwa asaletsedwe kulowa m'banja.



23 - **Ana** – Ana onse osakwanitsa zaka 18, alandire chithandizo chofanana ndi nkhani ya malamulo kosasala chifukwa chakuti adabadwira mchikwati kapena ayi. Anthu onse owonetsetse kuti akupanga zinthu zothandiza mwana. Ana onse azikhala ndi dzina ndipo azipatsidwa dzina lawolawo komanso la makolo ndipo azidziwika kuti ndi nzika kuno kapena kwina. Ana azidziwa makolo awo ndipo azileredwa ndi makolo posatengera kuti makolo awo adakwatirana kapena ayi kapena kuti makolowo adasiyana ukwati kapena ayi. Ndipo ana onse ayenera kutetezedwa posatengera kuti ndi ovutika, amasiye kapena olumala. Ana azitetezedwa ku ntchito iliyonse yomwe ingawononge matupi awo, ingawalepheretse maphunziro komanso ingawawonongere umoyo kapena kakulidwe ka mthupi, mu uzimu ndi umunthu wawo.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: KUPANGA ZOPINDULIRA MWANA

### Mwana asakhale nawo mndende ndi makolo ake

Mchigamulo cha mlandu wapakati pa *Alasoni ndi Boma*, Khothi La Likulu la Malawi lidanena kuti khothi liyenera kugamula mlandu uliwonse okhudza mwana mopindulira mwanayo. Mwanayo adatengedwa ku ndende ndi amayi ake pomwe adamangidwa, chifukwa palibe wina yemwe akadamulera kunja kwa ndende. Khothi lidagamula kuti kholo kapena mlezi wa mwana yemwe wamangidwa aliganizire zolipatsa belo msangamsanga pokana kuti mwanayo angazuzike mndendemo. Woweruzayo adati nkoyenera kuganizira mozama za mavuto omwe mwanayo angakumane nawo kamba ka kumangidwa kwa kholo lake.



(CREDIT: Achipungu)


24 – **Ufulu wa Amayi** - Amayi ali ndi ufulu wolandira chitetezo chokwanira mosasankha pa Malamulo, ndipo sikuloledwa kuti aziwasala chifukwa choti amayi kaya ali pabanja kapena ayi ndipo ufuluwo utanthauza kuti azilandira ufulu wonga wa amuna malinga ndi malamulo. Lamulo, miyambo ndi mchitidwe ulionse wosala amayi ku nyumba kaya ku ntchito, owazunza, wankhanza zamtundu uliwonse kuphatikizapo kuwalanda katundu wamasiye ndi zoletsedwa ndi Malamulo a Akulu adziko lino.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: KUGAWA KATUNDU MWACHILUNGAMO

### (Katundu agawidwe mwachilungamo pachisudzulo)

Mchigamulo cha mlandu wa *Rose Magombo v Luka Magombo*, Khothi lidagamula kuti chuma chapabanja chimakhala cha mwamuna ndi mkazi popeza onse okwatirana amathandizira kuti banja lawo liziyenda bwino, ndipo chuma cha banja chikuyenera kutengedwa kuti ndi cha onse. Izi zikutanthauza kuti chuma chiyenera kugawidwa mofanana, mosachenjeretsa mkazi nthawi ya chisudzulo. Khothi lidanenanso kuti mkazi asalandidwe chuma chamasiye mwamuna wake akamwalira.

25. **Maphunziro**- Munthu aliyense ali ndi ufulu wamaphunziro. Sukulu zomwe sizaboma ndizovomereka, koma ziyenera kulembetsedwa ku Boma.



## CHIPHUNZITSO: MUNTHU ALIYENSE ALI NDI UFULU WAMAPHUNZIRO

### Boma lidaika maphunziro awaulere ndi okakamiza kwa ana onse azaka zosakwana 18

Malamulo a Akulu amafotokoza mwachindunji kuti munthu aliyense ali ndi ufulu wamaphunziro. Pofuna kukwaniritsa ufuluwo, Gawo 13 la **Lamulo la Maphunziro,** limapereka ufulu wa sukulu yaulere m'masukulu a Boma. Lamulo la za maphunziro limakakamizanzo ana ochepera zaka 18 kuti akhale pasukulu. Aliyense ayenera kudziwa kuti sukulu zomwe sizaboma, zolipira ndi zololedwa, ndipo zimathandiza kuti aliyense akhale ndi mwayi wopeza maphunziro aulere pasukulu yaboma ngati akufuna.

26. **Chikhalidwe ndi chiyankhulo**- Munthu aliyense ali ndi ufulu wogwiritsa ntchito chinenero komanso chikhalidwe cha mtundu monga mwachifuniro chake.

27. **Ukapolo komanso kugwira ntchito mokakamizidwa**- Sikolelodwa kumsunga munthu muukapolo kaya mopysinjidwa. Ukapolo komanso malonda aukapolo saloledwa. Sikuloledwa kugwiritsa munthu ntchito mokakamiza.




28. **Katundu**- Munthu aliyense ali ndi ufulu wopeza katundu kapena chuma mwa iye yekha kapena mogwirizana ndi ena ndipo palibe angalindidwe katundu wake popanda chifukwa chokwanira chovomerezeka ndi malamulo.

29. **Ufulu wazachuma komanso chikhalidwe**- Aliyense ali ndi ufulu kugwira ntchito ndikupeza thandizo latsiku ndi tsiku.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WODZIPEZERA ZOSOWA PAMOYO

### Anthu ali ndi ufulu wodzipezera zosowa za pamoyo wawo

Mchaka cha 1993, boma lidaletsa azisudza kuchita zisudzo m'malo aboma zomwe zidalepheretsa anthu ena ochita zisudzo kugwira ntchito yawo yopezera ndalama. M'modzi mwa anthuwa a *Du Chisiza adakamang'alira Unduna wa Maphunziro ndi Chikhalidwe* womwe udaika chiletsochi ku khothi. Khoti lidagamula kuti boma lidalakwitsa pochita izi popeza lidalepheretsa anthu ena kugwira ntchito yawo yopezera ndalama popanda chifukwa chomveka bwino. Khothi lidatsindika kuti Boma lilibe mphamvu zotsekerezera ufulu wa anthu kugwira ntchito yawo yopezera ndalama zodzithandizira pamoyo watsiku ndi tsiku popanda chifukwa chokwanira.

30. **Ufulu wachitukuko-** Anthu onse ali ndi ufulu wopititsa patsogolo miyoyo yawo ndipo adzidyerera pa chuma, pa chikhalidwe ndi pa ndale, makamaka amayi, ana ndi onse olumala apatsidwe chithandizo chapadera chopititsa mtsogolo ufulu umenewu. Boma lidzipereke kuti ufulu wopititsa mtsogolo chitukuko udzioneka kuti ulipodi. Ndipo pa mfundo zothandiza pa ntchitotiyi pakhalenso kuonetsetsa kuti onse mosakondera ali ndi mwayi wopezera chuma, maphunziro, chithandizo pa umoyo wabwino, pogona pabwino, mwayi wokhala pantchito, komanso zithandizo zina monga misika, madzi ndi misewu. Boma lichitepo kanthu pakusintha zinthu kuti ena asatsalire m'mbuyo pothetsa zoperewera pa miyoyo ya anthu. Boma lili ndi udindo wolemekeza ufulu wa chitukuko ndipo lidziyeneraza Mfundo zoyendetsera dziko pachitukuko.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WA CHITUKUKO

**Kuteteza zinthu zofunikira pamoyo kumathandiza anthu kukhala ndi mwayi wokwaniritsa zomwe kuthekera kwawo.**

M'Malawi aliyense ali ndi ufulu wachitukuko. Ufuluwu ndiwofunikira kwambiri kwa anthu ovutika ndi uzunzika omwe amavutika kuti apeze zofunika zawo zatsiku ndi tsiku kuti atukule miyoyo yawo popanda thandizo la boma. Akaidi ndi limodzi mwamagulu a anthu omwe amavutika. Amavutika popeza amasungidwa ndi boma, amadyetsa ndi boma ndipo amadalira bomalo kuti aphunzire komanso apeze chithandizo cha za umoyo.

Mchigamulo cha mlandu wa *Masangano ndi Mkulu Woimira Boma pa Milandu*, andende angapo adakasuma ku Khothi kuti boma lidawaphwanyira ufulu polephera kuwapatsa zinthu zofunika pa moyo ngati chakudya chokwanira, mankhwala, zovala komanso kugona m'malo othithinana.

Khothi lidapeza kuti boma limawaphwanyira anthuwa ufulu polephera kupereka zinthu zofunika m'moyozi ndipo lidatsindika kuti zotere ndi zotsutsana ndi ulamuliro wa demokalase omwe umalemekeza ufulu wa anthu okhala ndi zofunika za moyo watsiku ndi tsiku. Khotilo ligamula kuti ufulu wa anthu omwe ali mndende wokhala moyo wabwino uyenera kutetezedwa ndi boma ndipo ufulu wokhala moyo wotukuka ndi wa anthu onse, ndipo aliyense amene ufulu wake waphwanyidwa atha kukadandaula ku Khothi.

31. **Ufulu wa pa ntchito** – Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala mwaubwino ndimosalidwa pa ntchito komanso kulipidwa malipiro oyenera. Aliyenese ali ndi ufulu wokhazikitsa ndikukhala membala wa bungwe loteteza mtendere pa ntchito kapena kusakhala membala ndikukana kupanga bungwe loteteza mtendere pa ntchito. Ufuluwu umaphatikizapo osasalidwa pa ntchito pachifukwa chilichonse komanso ufulu wonyanyala ntchito.



## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WOCHITIRIDWA CHILUNGAMO PANTCHITO

### Ntchito imayenera kutha mwachilungamo

Chigamulo cha mlandu *Granger Nkhwazi ndi Commercial Bank of Malawi Ltd*, Khothi la Likululi lidalamula kuti anthu olemba anthu ntchito asachotse antchito opanda chifukwa chenicheni komanso osatsatira ndondomeko yochotsera anthu ntchito. Izi zimathandiza kuti anthu asachotsedwe ntchito mwachisawawa ndi mopanda chilungamo

32. **Ufulu wolowa Mgwirizano-** Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala m'bungwe lililonse, zimene zimatanthauzanso ufulu wopanga bungwe. Palibe wina akakamize munthu kuti akhale m'bungwe lililonse.

33. **Ufulu wa maganizo-** Munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi maganizo ake, chipembedzo chake ndi chikhulupiriro chake, zolingalira komanso nzeru za maphunziro ake.

34. **Ufulu wamaganizidwe-** Munthu aliyense ali ndi ufulu woganizo monga mwa kufuna kwake ndipo angathe kusunga za kukhosi kake osamukakamiza kuti amve izi kapena aganize izi.

35. **Ufulu wolakhula za kukhosi-** Munthu aliyense ali ndi ufulu wolankhula zomwe akufuna.

36. **Ufulu wofalitsa nkhani-** Ofalitsa nkhani ali ndi ufulu wotola nkhani ndi kuzifalitsa momasuka, muno m'Malawi kapena kunja kwa dziko lino, ndipo azipatsidwa ufulu wopeza nkhani kuti athe kugwira ntchito yawo.



## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO: UFULU WA ATOLANKHANI, KUYANKHULA ZAKUKHOSI NDI MALINGALIRO NTHAWI ZAMBIRI UMALUMIKIZANA

### Boma silingaletse anthu kulankhula za kukhosi

Anthu osiyanasiyana ankapereka maganizo awo pa wailesi momwe chisankho cha 2019 chidayendera. Boma lidaletsa mawailesi kuulutsa mapulogalamu oterewa. Ofalitsa nkhani kudzera m'bungwe lawo adakasuma ku khothi. Mchigamulo cha mlanduwu wa pakati pa *Bungwe la boma loyanga'anira ntchito zofalitsa mawu (Malawi Communications Authority) ndi ena ndi Bungwe la atolankhani (National Media Institute of Southern Africa)* ndi ena, khothi lidati kuletsa mapulogalamu koteroku ndi kosaloledwa chifukwa ndi kuphwanya ufulu wolankhula za kukhosi womwe ndi nsanamira yaikulu ya ulamuliro wa demokalase yomwe sifunika kuchotsedwa mwachisawawa.

37. **Ufulu wopeza uthenga**- Munthu aliyense ali ndi ufulu wopeza nkhani iliyonse yosungidwa ndi Boma kapena nthambi yake iliyonse ngati nkhaniyo njofunika kuti munthuyo agwiritse ntchito ufulu wake.

38. **Ufulu wosonkhana ndi ena** – Munthu aliyense ali ndi ufulu wokumana ndi anzake ndi kuchita nawo chiotsero chakukhumudwitsidwa ndi nkhani iliyonse mogwirizana ndi anzakewo koma mopanda ziwawa ndiponso mosakgwiritsa ntchito zida.



## CHIPHUNZITSO: ALIYENSE ATHA KUCHITA CHIONETSERO

### Zionetsero zisingaletsedwe wamba ndi boma

Mchaka cha 2002, Mtsogoleri wa Dziko lino adaletsa ziwonetsero zonse zotsutsana ndi malingaliro osintha Malamulo a Akulu kuti Mtsogoleri azitha kusankhidwa pa zisankho kodutsira kawiri. Bungwe la maloya la Malawi Law Society lidakasuma ku khothi pa mlandu wa *Malawi Law Society ndi ena ndi Mtsogoleri wa dziko ndi ena* ndipo Khoti La Likulu lidagamula kuti kuletsa zionetseroku kunali kuphwanya ufulu wa anthu ochita zionetsero. Khothilo lidatinso Mtsogoleri wa Dziko sangaletse zionetsero chifukwa chakuti sizikumusangalatsa koma ziwonetsero zitha kuletsedwa ngati zingabweretse ziwawa kapena upandu ulionse.

39. **Ufulu woyenda komanso malo wokhala-** Munthu aliyense ali ndi ufulu wopita kulikonse ndi kukhala malo aliwonse m'Malawi muno. Munthu ali ndi ufulu wotuluka kunja kwa Malawi ndikubweranso.

**4**0. **Ufulu wochita ndale-** Munthu aliyense ndi ufulu wokhazikitsa kulowa, ndi kuchita nawo ndale kuphatikizanso kukopa anthu kuti alowe chipani chandale. Aliyense ali ndi ufulu wotenga nawo gawo pa ndale, kuvota mwachinsinsi pa chisankho ndi kuima nawo pa chisankhocho.

## CHIPHUNZITSO MCHIGAMULO : ALIYENSE ALI NDI UFULU WOPONYA VOTI

### Ufulu wovota ku Malawi utetezedwe

Ufulu woponya voti wazikizira ku Malawi kuno chisinthireni ndale mchaka cha 1993. Komachisankho cha mchaka cha 2019, sichidayende bwino popeza panali zovuta zosiyanasiyana pa kawerengedwe ka mavoti. A Chilima ndi a Chakwera omwe adaima nawo pa chisankhochi adakamang'ara ku Khothi kutsutsana ndi zotsatira za zisankhozo pa *Mlandu wa Chilima ndi Chakwera ndi Mutharika ndi Bungwe la Chisankho*. Khothi lidazikizira pa mfundo yakuti "mphamvu yoyendetsa boma ikhalepo ngati chikhulupiriro cha anthu chikupitirirabe pa Boma lawo, ndipo chikhulupirirochi chitha kupitirira ngati zinthu zikuchitika poyera, motsata zofuna anthu popanda kuwabisira." Khothi lidapeza kuti zotsatira za chisankho cha 2019 zinali zosavomerezeka komanso zosadalilika kuti ndi mmene anthu adaponyera voti.

Chigamulo cha mlanduwu chikuonetseratu kufunika kwa chisankho ndi voti mu ulamuliro wa demokalase. Uwu ndi ufulu umene umawapatsa a Malawi ufulu osankha atsogoleri omwe akuwakhulupirira ndipo akufuna aziwalamulira.

41 **- Kupezeka kwa chilungamo ndi chithandizo chovomerezeka–** Munthu aliyense ali ndi ufulu wadandaula ku Khothi lililonse kapena ku Bungwe lililonse lofufuza ndi kuweruza mlandu wake.

42 - **Kumangidwa, kusungidwa ndi kuweruzidwa mwachilungamo-** Ngati wina wamangidwa, ayenera kuuzidwa chifukwa chomwe wamangidwira. Munthu ayenera kumangidwa mndende za ukhondo ndi zosamalika bwino zomusungira ulemu. Ndipo ayenera kulandira zinthu polemba ndi zolembera ndi zowerenga ngati angafune. Boma liyenera kumupatsa chakudya chokwanira, ndi chithandizo chamankhwala chomwe amafunikira. Munthu aliyense womangidwa ali ndi ufulu wokumana ndi kukambirana ndi Woyimira anthu pamilandu (Loya) pa mlandu wake, ndipo ayenera kuuzidwa za ufuluwu msangamsanga atangomangidwa. Ali ndi ufulu wopatsidwa loya ndi Boma ngati mlandu wake ndi wofunika kuti akhale ndi loya koma iyeyo sangakwanitse kudzipezera loyayo. Munthu aliyense yemwe wamangidwa ali ndi ufulu wolankhulana ndi mkazi wake kapena mwamuna wake kapena wachibale wake, mlangizi wachipembedzo komanso dototolo yemwe wasankha. Aliyense ayenera kukhala ndi mpata wofunsa Khothi kuti liwunike bwino zakumangidwa kwake, ndipo ayenera kumasulidwa ngati kumangidwa kwake kuli kosaloledwa. Wina akamangidwa, ayenera kuwuzidwa kuti ali ndi ufulu wokhala chete, ndi kukawonekera kukhothi asanathe maola 48 chimangidwireni. Palibe amene ayenera kukakamizidwa kuvomereza kapena kunena chilichonse chomwe chingagwiritsidwe ntchito ngati umboni wotsutsana naye. Anthu omwe akuimbidwa mlandu, ndipo akudikirira kuti aweruzidwe akuyenera kusungidwa padera; mosaphaitikizana ndi anthu omwe adapezeka kale wolakwa pa milandu yawo. Aliyense ali ndi ufulu uwoweruzidwa mwachilungamo, ndipo izi zikuphatikiza ufulu woweruzidwa pagulu, kubwalo la milandu lodziyimira palokha komanso losakondera, kuuzidwa mlandu womwe akuimbidwa, kutengedwa ngati munthu wolakwa khothi lisanagamule kuti ndi wolakwa, komanso kukhala chete, kukhala ndi womuyimirira, kuti asapezeke olakwa pamlandu womwewo kawiri, ndi kuzenga mlandu wawo mchiyankhulo chomwe amachimva, kapena kuti mlanduwo umasuliridwe ndi omasulira yemwe amalipidwa ndi boma. Anthu omwe sanakwanitse zaka 18; ana, ali ndi ufulu wapadera, kuphatikiza ufulu wosawalamula kuti akhale m'ndende moyo wawo wonse, kumangidwa mosiyana ndi akulu, ndi kuchitiridwa zinthu zolandira chilango choyenera msinkhu wawo komanso chothandizira kuti akadzatuluka adzakhale nzika yodaliririka.



(CREDIT: Lizel Louw)

## CHIPHUNZITSO: UFULU WOCHITA ZINTHU MOMASUKA UMATHANDIZA KUTETEZA ULEMU WA ANTHU

### Kuperewera kwa ufulu kuyerenera kuchitika pokhapokha ntchito zoweluza milandu zikayendetsedwa bwino komanso mwachilungamo

Pa nkhani ya *Pempho Banda*, Khoti La Likulu lidatsimikiza kuti aliyense akuyenera kuweruzidwa mwachilungamo, kuti aliyense akuyenera kuchitiridwa chilungamo ndi ndondomeko yolongosola zachilungamo. Izi zikutanthauza kuti chilichonse pamlandu chikuyenera kuchitika mwachilungamo. Pa nkhani iyi, panali zinthu zingapo zomwe zimatanthauza kuti mlanduwo sudachitike mwachilungamo ndipo padalibe amene adakapezeka wolakwa.

43. **Kayendetsedwe kantchito-** Ziganizo zomwe zimakhudza anthu ziyenera kukhala zachilungamo komanso zovomerezeka, zounika ufulu, kumasulidwa ndi zokhumba zomwe wina alinazo. Adindo ayenera kufotokozera anthu omwe ufulu wawo ndi machitidwe ali onse a Boma.



(CREDIT: IFPRI)

# KUUMBA MKOTA

Malamulo a Akulu oyendetsera dziko lino ali ndi masomphenya otukula miyoyo ya a Malawi. Ufulu wachibadwidwe ndi njira imodzi yokwaniritsira masomphenyawa. Boma lili ndi udindo waukulu wowonetsetsa kuti ufulu wachibadwidwe wazikizira muno m'Malawi. Aliyense wa ife atengepo gawo polondoloza kuti boma likwaniritse masomphenyawa.


(CREDIT: Swathi Sridharan (ICRISAT))

# MABUNGWE OTETEZA MUTETEZE UFULU WACHIBADWIDWE

**Bungwe lothana ndi Katangale (Anti-Corruption Bureau)**
Bungwe lothana ndi Katangale ndi bungwe la boma lomwe limalimbana ndi mchitidwe wa katangale ndipo limafufuza madandaulo aliwonse a katangale ndi kuimba mlandu anthu ochita katangale. Bungweli limalimbana ndi katangale wa mabungwe aboma komanso omwe si aboma. Iwo mungawapeze motere:-
Komwe akupezeka: Mulanje House, City Centre, Lilongwe
Keyala : P.O Box 2437, Lilongwe
Nambala ya Foni: +265(0)888 208 963 kapena +265(0) 1 770 166
Imelo: reportcentre-ll@acbmw.org
Tsamba la Intaneti: https://acbmw.org/
Twita: @ ACBMalawi

**Makhothi**
Makhothi amateteza ufulu wa anthu pozenga milandu ina iliyonse kuphatikizapo yophwanya ufulu. Iwo mungawapeze motere:-
Likulu la Ofesi yawo : Judiciary Premises, Chichiri, pafupi ndi Koleji ya Polytechnic, Blantyre
Keyala: P.O Box 30244, Chichiri, Blantyre 3
Nambala ya Foni: +265 187 0255 kapena +265 1873873
Imelo: malawijudiciary@judiciary.mw or highcourt@judiciary.mw
Tsamba la Intaneti: https//: www.judiciary.mw/

**Bungwe Loteteza Ufulu wa Anthu (Malawi Human Rights Commission)**
Ili ndi bungwe loyang'anira ufulu wachibadwidwe ku Malawi ndipo ndi lodziyimira palokha. Ntchito yake ndi kuteteza komanso kufufuza za kuphwanyidwa kwa ufulu wachibadwidwe wa anthu. Iwo mungawapeze motere;-
Likulu la Ofesi yawo: H.B. House, mu msewu wa Paul Kagame Road, Lilongwe
Keyala: Private Bag 378, Lilongwe
Nambala ya Foni: +265 1 750 900 (Lilongwe)/+265 1 83 945 (Blantyre)
Imelo: info@mhrcmw.org
Tsamba la Intaneti: https://www.mhrcmw.org/

**Ombudzimani (Ombudsman)**

Ombudzimani ndi ofesi yomva ndi kufufuza madandaulo a anthu omwe ufulu wawo waphwanyidwa ndi boma kapena nthambi iliyonse ya Boma ndipo munthu odandaulayo sangapezenso chithandizo kulikonse. Iwo mungawapeze motere;-

Likulu la Ofesi yawo : St Martin's House, pafupi ndi Teveta House, Lilongwe

Keyala: Private Bag 348, Capital City, Lilongwe

Nambala ya Foni: +265 1 77 4899 or +265 1 77 4866

Imelo: ombudsman@ombudsmanmalawi.org

Tsamba la Intaneti: http://mw.ombudsmanmalawi.org/